



ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2026 – 2027

UNDUNA WA ZACHILENGEDWE
Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo


BLANTYRE
DISTRICT

Mwachidule

Nyengo ya dzinja ya 2026-2027 ikuyembekezeka kukhudzidwa **ndi El Nino wa mphamvu**. El Nino ndi kutentha kopyola muyezo kwa madzi m'dera la pakati chakum'mawa kwa Nyanja ya mchere ya Pacific komwe kamakhudza kagwedwe ka mvula dziko lonse.

Blantyre akuyembekezereka kulandira mvula ya **mlingo wokhazikika kapena kuchepera apo** mu dzinja la 2026-2027.

October 2026




Mwezi wa October ukuyembekezereka kutentha ndi mwayi wa mvula ya Chizimalupsa

Mvulayi idzakhala yotsogozana ndi mphepo ya mkuntho komanso ziphaliwali

November 2026


November 2026 Rainfall Forecast



Mvula ya mlingo wa pakati pa 50-100mm ikuyembekezereka m'madera ambiri. Mvulayi idzakhala ya mphepo ya mkuntho komanso mphezi.

December 2026

December 2026 Rainfall Forecast




Madera ambiri akuyembekezereka kulandira Mvula ya mlingo wa pakati pa 200-250mm. Malo ochepa a TA Kuntaja ndi TA Kunthembwe adzalandira mlingo wa pakati pa 100-150mm.

Mvula ikuyembekezereka kukhazikika pakati pa mwezi wa December

January 2027

January 2027 Rainfall Forecast




Mvula ya mlingo wokhazikika kapena wochepera apo ikuyembekezeka. Koma madera ena akwa TA Kuntaja, Kunthembwe ndi Kapeni akuyembekezereka kulandira mvula yocheperako.

Ng'amba ya sabata imodzi ikuyembekezereka mu mweziwu.

February 2027

February 2027 Rainfall Forecast




Mwezi wa February, mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuchepera apo ikuyembekezereka m'madera ambiri. Mvulayi idzakhala ya pakati pa 100-150 mm.

Pali kuthekera kwa ng'amba yofikira masabata awiri m'mweziwu.

March 2027

March 2027 Rainfall Forecast




Mvula ya mlingo wokhazikika Kapena kuposera apo ya mlingo wa 150-200mm ikuyembekezereka.

Komabe madera ena opezeka kumwera kwa bomali ali ndi kuthekera kolandira mvula yambiri.

April 2027

April 2027 Rainfall Forecast



Mvula ya mulingo wapakati pa 50mm ndi 100mm omwensu ndi mlingo wokhazikika kapena kuchepera apo ikuyembekezereka m'mwezi wa April.

Mvula ikuyembekezeka kufika kumapeto sabata yachiwiri ya April 2027.

DZINJA MWACHIDULE

MVULA YOKHAZIKIKA

Ikuyembekezeka kuyamba sabata yachiwiri m'mwezi wa December

NG'AMBA

Sabata imodzi mu mwezi wa January komanso masabata awiri mu February.


KUTALIKA KWA DZINJA

Nyengo ya dzinja ya ikuyembekezeka kukhala ya masiku 115 - 125

MATHELO A MVULA

Sabata yachiwiri ya mwezi wa April

MONTH	NORMAL RANGE	FORECAST
OCT	12.9	39.7
NOV	76.0	128.8
DEC	184.0	263.4
JAN	240.6	306.6
FEB	193.1	294.6
MAR	137.5	181.3
APR	32.3	85.6



Chithunzi ichi chapereka ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:



Tsatilani ulosi ndi malangizo ochokera ku nthambi yoona zanyengo



For further information contact:

The Director of Climate Change and Meteorological Services,
P.O. Box 1808, Blantyre.



+265 991 69 00 61



metdept@metmalawi.gov.mw



www.metmalawi.gov.mw